## TINGADZIWE BWANJI KUTI NDIFE OPULUMUTSIDWA?

Baibulo likunena momveka kuti tingadziwe kuti ndife wopulumutsidwa. 1 Yohane 5:13 akuti *"Izi ndikulemberani, kuti* ***mudziwe*** *kuti muli ndi moyo wosatha, inu amene mukhulupirira dzina la Mwana wa Mulungu."* Funso ndi ili: Cholembedwa ndi chani kuti tidziwe kuti ndife opulumutsidwa?

Pa Machitidwe 2:38 ndi Aefeso 1:13 mawu akuti tikalapa ndi kukhulupirira, timalandira Mzimu Woyera ndipo vesi lotsatirali likuti, kudzera mwa Mzimu, tingathe kudziwa kuti ndife opulumutsidwa. 1 Yohane 4:13 akuti *"m'menemo tizindikira kuti tikhala mwa Iye, ndi Iye mwa ife, chifukwa anatipatsako Mzimu wake."* Kuchokera pa vesi imeneyi, tikuona kuti chitsimikizo cha chipulumutso chathu ndiko kupezeka kwa Mzimu wa Yesu mu Moyo wathu.

## KODI MZIMU ANGATHE KUPEZEKA MWA IFE BWANJI?

Tingathe kuwerenga kuti tinapatsidwa Mzimu, koma ***timazindikira*** kuti Mzimu ali mu moyo wathu? Aroma 8:14 akuti *"Pakuti onse amene atsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu, amenewo ali ana a Mulungu."* Choncho tingadziwe kupezeka kwa Mzimu wa Mulungu mwa ife chifukwa amatitsogolera komanso kutifulumiza kukhala moyo wa chiyero. Titatsatira kulankhula kwa Mzimu mkati mwathu, tidzasinthika ndipo mawu opezeka pa 2 Akorinto 5:17 adzakhala owona mu moyo wathu. Vesili likuti, *"Chifukwa chake ngati munthu ali yense ali mwa Khristu ali wolengedwa mwa tsopano; zinthu zakale zapita, taonani, zakhala zatsopano."* Izi zimachitika pamene Mzimu wa Mulungu atitsogolera ife kusiya moyo wa uchimo ndi kukhala obadwa watsopano mu moyo watsopano okondweretsa Mulungu.



## KODI MZIMU ANGATHE KUTITSOGOLERA KUMOYO WATSOPANO BWANJI?

Pamene tilandira Mzimu Woyera mu moyo wathu, sitimakhala woyera mtima wopanda tchimo, koma chomwe chimachitika ndi ichi: machimo amakhululukidwa ndipo Mzimu amatipatsa mphamvu yokana tchimo lamtsogolo, ndipo timakhala moyo wa chiyero.

Zokhudza Mzimu, Yohane 16:8 akuti: *"Ndipo atadza Iyeyo adzatsutsa dziko lapansi za machimo, ndi za chilungamo, ndi za chiweruzo."* Pamene Mzimu atitsutsa ku tchimo, timakhala otsutsika, osowa mtendere, ndipo izi zimatitsogolera ku kulapa, kulandira chikhululukiro, komanso kuyeretsedwa. 1 Yohane 1:9 akuti: *"Ngati tivomereza machimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama Iye, kuti atikhululukire machimo athu, ndikutisambitsa kutichotsera chosalungama chiri chonse".* Mwa ichi, timakhululukidwa komanso kuyeretsedwa ku tchimo ndipo timakhala ndi moyo wosatha. 2 Atesalonika 2:13 amanena kuti tinapulumutsidwa mwa chiyeretso cha Mzimu.

## CHINGACHITIKE NDI CHIYANI NGATI SITIMVERA KUTSUTSIDWA KWA MZIMU?

Aroma 8:12-13 akuti: *"… Abale ife tiri amangawa … Ngati mukhala ndi moyo monga mwathupi, mudzafa, koma ngati ndi mzimu, mufetsa zochita zake za thupi, mudzakhala ndi moyo."* Tiri ndi udindo kutsatira chitsogozo cha Mzimu, apo ayi tidzafa (tidzapita ku Gehena).

Buku la 1 Yohane likuti munthu yemwe wabadwa mwa Mulungu sapitilira kuchimwa. 1 Yohane 3:6-10 akuti: *"yense wakukhala mwa Iye sachimwa … iye wochita tchimo ali wochokera kwa mdierekezi … Yense wobadwa kuchokera kwa Mulungu sachita tchimo chifukwa mbeu yake ikhala mwa iye.*

## TINGADZIWE BWANJI KUTI NDIFE OPULUMUTSIDWA?

Baibulo likunena momveka kuti tingadziwe kuti ndife wopulumutsidwa. 1 Yohane 5:13 akuti *"Izi ndikulemberani, kuti* ***mudziwe*** *kuti muli ndi moyo wosatha, inu amene mukhulupirira dzina la Mwana wa Mulungu."* Funso ndi ili: Cholembedwa ndi chani kuti tidziwe kuti ndife opulumutsidwa?

Pa Machitidwe 2:38 ndi Aefeso 1:13 mawu akuti tikalapa ndi kukhulupirira, timalandira Mzimu Woyera ndipo vesi lotsatirali likuti, kudzera mwa Mzimu, tingathe kudziwa kuti ndife opulumutsidwa. 1 Yohane 4:13 akuti *"m'menemo tizindikira kuti tikhala mwa Iye, ndi Iye mwa ife, chifukwa anatipatsako Mzimu wake."* Kuchokera pa vesi imeneyi, tikuona kuti chitsimikizo cha chipulumutso chathu ndiko kupezeka kwa Mzimu wa Yesu mu Moyo wathu.

## KODI MZIMU ANGATHE KUPEZEKA MWA IFE BWANJI?

Tingathe kuwerenga kuti tinapatsidwa Mzimu, koma ***timazindikira*** kuti Mzimu ali mu moyo wathu? Aroma 8:14 akuti *"Pakuti onse amene atsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu, amenewo ali ana a Mulungu."* Choncho tingadziwe kupezeka kwa Mzimu wa Mulungu mwa ife chifukwa amatitsogolera komanso kutifulumiza kukhala moyo wa chiyero. Titatsatira kulankhula kwa Mzimu mkati mwathu, tidzasinthika ndipo mawu opezeka pa 2 Akorinto 5:17 adzakhala owona mu moyo wathu. Vesili likuti, *"Chifukwa chake ngati munthu ali yense ali mwa Khristu ali wolengedwa mwa tsopano; zinthu zakale zapita, taonani, zakhala zatsopano."* Izi zimachitika pamene Mzimu wa Mulungu atitsogolera ife kusiya moyo wa uchimo ndi kukhala obadwa watsopano mu moyo watsopano okondweretsa Mulungu.



## KODI MZIMU ANGATHE KUTITSOGOLERA KUMOYO WATSOPANO BWANJI?

Pamene tilandira Mzimu Woyera mu moyo wathu, sitimakhala woyera mtima wopanda tchimo, koma chomwe chimachitika ndi ichi: machimo amakhululukidwa ndipo Mzimu amatipatsa mphamvu yokana tchimo lamtsogolo, ndipo timakhala moyo wa chiyero.

Zokhudza Mzimu, Yohane 16:8 akuti: *"Ndipo atadza Iyeyo adzatsutsa dziko lapansi za machimo, ndi za chilungamo, ndi za chiweruzo."* Pamene Mzimu atitsutsa ku tchimo, timakhala otsutsika, osowa mtendere, ndipo izi zimatitsogolera ku kulapa, kulandira chikhululukiro, komanso kuyeretsedwa. 1 Yohane 1:9 akuti: *"Ngati tivomereza machimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama Iye, kuti atikhululukire machimo athu, ndikutisambitsa kutichotsera chosalungama chiri chonse".* Mwa ichi, timakhululukidwa komanso kuyeretsedwa ku tchimo ndipo timakhala ndi moyo wosatha. 2 Atesalonika 2:13 amanena kuti tinapulumutsidwa mwa chiyeretso cha Mzimu.

## CHINGACHITIKE NDI CHIYANI NGATI SITIMVERA KUTSUTSIDWA KWA MZIMU?

Aroma 8:12-13 akuti: *"… Abale ife tiri amangawa … Ngati mukhala ndi moyo monga mwathupi, mudzafa, koma ngati ndi mzimu, mufetsa zochita zake za thupi, mudzakhala ndi moyo."* Tiri ndi udindo kutsatira chitsogozo cha Mzimu, apo ayi tidzafa (tidzapita ku Gehena).

Buku la 1 Yohane likuti munthu yemwe wabadwa mwa Mulungu sapitilira kuchimwa. 1 Yohane 3:6-10 akuti: *"yense wakukhala mwa Iye sachimwa … iye wochita tchimo ali wochokera kwa mdierekezi … Yense wobadwa kuchokera kwa Mulungu sachita tchimo chifukwa mbeu yake ikhala mwa iye.*

***M'menemo aoneka ana a Mulungu, ndi ana a mdierekezi: yense wosachita chilungamo siali wochokera mwa Mulungu, ndi iye wosakonda m'bale wake."***

Palibe angapulumuke kwa muyaya polapa kwa kanthawi ndikubwereranso mu uchimo. Izi zingakhale ngati kunena kwa Yesu kuti: "ZikomoYesu pondipulumutsa. Ndikubwerera ku moyo wanga wakale koma ndikudziwa kuti mwandikhululukira machimo anga akale, atsopano komanso amtsogolo." Machimo amtsogolo amayenera kuvomerezedwa komanso kulapa. Tikuyenera, kudzera mu mphamvu ya Mzimu Woyera, kukhala moyo wokodweretsa Mulungu chifukwa Aheberi 12:14 akuti: *"Opanda chiyero palibe m'modzi adzaona Ambuye."* Moyo wa uchimo utanthauza: kunama, miseche, kuba, kuledzera, kuzonda mbale wako, kusilira, chidetso, kuwawidwa mtima komanso mkwiyo. Sitingakhale moyo wopanda tchimo, koma tikuyenera, kudzera mwa mzimu, kukhala moyo wodziletsa kuchita tchimo mwadala. Kupanda apo, tidzafa. Agalatiya 5:16

**CHONCHO, UNGADZIWE BWANJI KUTI NDIWE OPULUMUTSIDWA?**

Yohane 3:3 Yesu akuti: *"Ngati munthu sabadwa mwatsopano, sakhoza kuona ufumu wa Mulungu."* Ngati munalapa tchimo, ndikumupempha Yesu kukhala Ambuye wanu, ndinu wobadwa mwatsopano. Muyenera ***kumva*** kupezeka kwa Mzimu Woyera mu moyo wanu pamene akutsutsani ku tchimo (Yohane 16:8) ndipo pamene muvomereza machimo anu, muzakhululukidwa, ndikuyeretsedwa, ndipo mtendere wa Mulungu uzabwereranso mu moyo wanu. Kupezeka kwa Mzimu Woyera kumapereka mphamvu yoti tiyende mu chiyero ndipo **MAYENDEDWE AMENEWA**, ndicho chitsimikizo cha chipulumutso chathu.

1 Yohane 5:3; 3:23 akuti: *"Ichi ndi chikondi cha Mulungu kuti tisunge malamulo ake … Ndipo lamulo lake ndi ili kuti tikhulupirire dzina la mwana wake Yesu Khristu, ndikukondana wina ndi mzake, monga anatilamulira."* Pamene mzimu atiyeretsa ku tchimo, lamulo loti timukonde Mulungu, limakhala zenizeni pa moyo wathu.

Aroma 13:10 akuti: ***"Chikondano chiri chokwaniritsa lamulo."***

Contact: Pastor Sam D Phiri
Cell phone: 088 415 7558 or 099 356 4671
Email: samdinala@yahoo.com

Written by:
Mick Alexander
leeandmick@gmail.com
www.ChristianIssues.biz

# Tingadziwe Bwanji Kuti Ndife Opulumutsidwa?

*"Izi takulemberani, kuti mudziwe kuti muli ndi moyo wosatha, inu amene mukhulupirira dzina la Mwana wa Mulungu."* 1 Yohane 5:13

***M'menemo aoneka ana a Mulungu, ndi ana a mdierekezi: yense wosachita chilungamo siali wochokera mwa Mulungu, ndi iye wosakonda m'bale wake."***

Palibe angapulumuke kwa muyaya polapa kwa kanthawi ndikubwereranso mu uchimo. Izi zingakhale ngati kunena kwa Yesu kuti: "ZikomoYesu pondipulumutsa. Ndikubwerera ku moyo wanga wakale koma ndikudziwa kuti mwandikhululukira machimo anga akale, atsopano komanso amtsogolo." Machimo amtsogolo amayenera kuvomerezedwa komanso kulapa. Tikuyenera, kudzera mu mphamvu ya Mzimu Woyera, kukhala moyo wokodweretsa Mulungu chifukwa Aheberi 12:14 akuti: *"Opanda chiyero palibe m'modzi adzaona Ambuye."* Moyo wa uchimo utanthauza: kunama, miseche, kuba, kuledzera, kuzonda mbale wako, kusilira, chidetso, kuwawidwa mtima komanso mkwiyo. Sitingakhale moyo wopanda tchimo, koma tikuyenera, kudzera mwa mzimu, kukhala moyo wodziletsa kuchita tchimo mwadala. Kupanda apo, tidzafa. Agalatiya 5:16

**CHONCHO, UNGADZIWE BWANJI KUTI NDIWE OPULUMUTSIDWA?**

Yohane 3:3 Yesu akuti: *"Ngati munthu sabadwa mwatsopano, sakhoza kuona ufumu wa Mulungu."* Ngati munalapa tchimo, ndikumupempha Yesu kukhala Ambuye wanu, ndinu wobadwa mwatsopano. Muyenera ***kumva*** kupezeka kwa Mzimu Woyera mu moyo wanu pamene akutsutsani ku tchimo (Yohane 16:8) ndipo pamene muvomereza machimo anu, muzakhululukidwa, ndikuyeretsedwa, ndipo mtendere wa Mulungu uzabwereranso mu moyo wanu. Kupezeka kwa Mzimu Woyera kumapereka mphamvu yoti tiyende mu chiyero ndipo **MAYENDEDWE AMENEWA**, ndicho chitsimikizo cha chipulumutso chathu.

1 Yohane 5:3; 3:23 akuti: *"Ichi ndi chikondi cha Mulungu kuti tisunge malamulo ake … Ndipo lamulo lake ndi ili kuti tikhulupirire dzina la mwana wake Yesu Khristu, ndikukondana wina ndi mzake, monga anatilamulira."* Pamene mzimu atiyeretsa ku tchimo, lamulo loti timukonde Mulungu, limakhala zenizeni pa moyo wathu.

Aroma 13:10 akuti: ***"Chikondano chiri chokwaniritsa lamulo."***

Contact: Pastor Sam D Phiri
Cell phone: 088 415 7558 or 099 356 4671
Email: samdinala@yahoo.com

Written by:
Mick Alexander
leeandmick@gmail.com
www.ChristianIssues.biz

Tingadziwe Bwanji Kuti Ndife Opulumutsidwa?

*"Izi takulemberani, kuti mudziwe kuti muli ndi moyo wosatha, inu amene mukhulupirira dzina la Mwana wa Mulungu."* 1 Yohane 5:13